

1 Yohane : 3:8-16

Mutu : Makhalidwe awiri a munthu wokhulupirira

Ndipereka moni wa Kumwamba kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero Ambuye afuna kutitsogolera ndi mau ake apa Mateyu 5:11, pamene Ambuye Yesu akunena kuti, “Odala muli inu m’mene adzanyazitsa inu, nadzazunza inu, nadzakunenerani monama zoipa ziri zonse chifukwa cha Ine.”

Mupologalamu yapita ija, tinali kukambirana pa 1 Yohane 3:1-9, pamene timapitiliza kuona za chikondi cha Atate kwa ana ake. Ndipo lero pa 1 Yohane 3:8-12, tiona makhalidwe awiri a munthu wokhulupirira.

8. Iye wochita tchimo ali wochokera mwa mdierekezi, chifukwa m’dierekezi anachimwa kuyambira pachiyambi.

Tiyeni poyamba tigwire mau akuti, “Iye wochita tchimo ali wochokera mwa m’dierekezi.” Pa mau amenewa, ndifuna tidziwe kuti m’dierekezi ndiye amene anadza ndi tchimo m’dziko lapansi. Tikunena kuti ndiye amene anakopa makolo athu oyamba kuti agwe mutchimo. Tere kuti inu ndi ine, tikhale ndi makhalidwe oipa

ndichifukwa cha satana. Kutsimikiza mau a Yohane amene akuti, “iye wochita tchimo ali wochokera mwa mdierekezi.” Mukumbukira Ambuye Yesu pa Yohane 8:44, adauza akulu achipembedzo kuti, “Inu muli wochokera atate wanu mdierekezi, ndipo zolakalaka zake za atate wanu mufuna kuchita.”

Wokondedwa anzanga apaulendo, pamau amenewa tikuona chinthu chochititsa chidwi chakuti ife, tiyenera kutengera makhalidwe ya atate wathu kapena kuti mwana ayenera kufanana ndi atate wake. Tere ngati inu atate wanu ndi mdierekezi, makhalidwe anu adzafanana ndi atate wanuyo. Ndipo ngati Atate wanu ndi Yehova, makhalidwe anonso adzafanana naye.

Tsono ganizo lachiwiri likuti satana anachimwa kuchokera pachiyambi kotero kuti wakhala akuchita tchimo kufikira lero lino. Iyeyu ndiye woukira Mulungu. Ndiye pachifukwa cha uchimo womwe udalowa m'dziko lapansi, tikuona kuti Mwana wa Mulungu anadza ndi cholinga chakuti athyoleufumu ndi ntchito zonse za mdierekezi. Pachifukwa chimenechi tipeza kuti ndi Yesu yekha yemwe angakumasulireni inu kumphamvu yauchimo, osati munthu ayi. Tikunena kuti pamene inu mwathinidwa ndi uchimo

muyenera kudza kwa m'sing'anga Wamkulu amene ali ndi mphamvu yothana ndi tchimo lina lililonse.

Wokondedwa, nkhani ikulozera inu kwa Ambuye Yesu yemwe anafa chifukwa cha machimo a dziko lapansi. Ichi, ndichimene Yohane m'batizi amatanthauza pa Yohane 1:29, pamene anati, "Onani Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo lake la dziko lapansi!" Kutanthauza kuti ndi Ambuye Yesu Kristu amene anatenga chilango cha machimo anu ndi anga. Ndiye pamene inu mukhulupirira Iye, machimo anu sakhalanso pa inu popeza mwapululumutsidwa kudzera mwa Kristu. Tsono pali chitsimikizo chakuti popeza inu mwalandira chipulumutso mwanjira yakuika chikhulupiriro chanu mwa Kristu, ndiye kuti machimo anu onse akwilidwa, kotero kuti sadzawerengedwanso pa inu.

Tsono Yohane mundime ino, akunena kuti Ambuye Yesu sadangochotsa tchimo lathu, koma anaonetsedwa kuti akhoza kuchotsa machimo athu onse. Iyeyu analibe tchimo linalililonse monga akunena Paulo pa Ahebri 7:26, pamene akuti, "Pakuti mkulu wa ansembe wotere anatiyenera ife, woyera mtima, wopanda choipa, wosadetsedwa, wosiyana ndi ochimwa..." Koma Iyeyu anali

munthu ndithu, ndipo anafa monga nsembe yathu yoperekedwa chifukwa cha machimo athu, kulipa dipo la machimo athu. Tsono Yohane pa verse 5, akuti, “Iyeyu anaonekera kudzachotsa machimo...” akutanthauza kuti Kristu anadza kudzachotsa machimo ya anthu wokhulupirira. Mwanjira ina Yohane akunena kuti Kristu anadza ndi cholinga chakuti inu ndi ine, tikhale ndi kuthekera kokhala ndi kuyenda m’moyo woyenera wachikristu.

Tsono nkhani iyi, ndiyomwe yatifikitsa pamutu wakuti wokhulupirira aliyense ali ndi makhalidwe awiri. Ili, ndilo lingaliro lomwe Paulo pa Aroma 7:19, akuti, “Pakuti chabwino chimene ndichifuna, sindichichita; koma choipa chimene sindichifuna, chimenechi ndichita.” Pamene Paulo akunena kuti “chabwino chomwe afuna kuchichita” akukamba za makhalidwe ake atsopano. Ndipo pamene akuti, “koma choipa, chimene sindichifuna...” akunena za makhalidwe ake akale kuti ndiwo amene amakhala ndi mphamvu pathupi lake. Kutanthauza kuti makhalidwe atsopano akafuna kuchita kanthu kabwino pamoyo wamunthu, makhalidwe akale amakhala ndi mphamvu yokokera thupi m’mbuyo. Kutsimikiza kuti umunthu wathu wakale sungatumikire Mulungu,

popeza ndiwo woukira Mulungu. Apa, akunena kuti palibe munthu angatumikire Mulungu ndi umunthu wakale pokha-pokha abadwense mwatsopano. Kutsindika mau amene akunena Yohane akuti, “Mwana wa Mulungu adaonekera, ndiko kuti akaononge ntchito za m’dierekezi.” Kutanthauza kuti Kristu anadza kuononga ntchito za m’dierekezi ndi cholinga chakuti inu ndi ine, tikakhale womvera Mulungu. Kodi inu, mumamvera Mulungu m’moyo wanu wachikristu?

9. Yense Wobadwa kuchokera mwa Mulungu sachita tchimo, chifukwa mbeu yake ikhala mwa iye; ndipo sakhoza kuchimwa, popeza wabadwa kuchokera mwa Mulungu.”

Yohane pano akukamba za kubadwa mwatsopano. Ichi, ndichimene Ambuye pa Yohane 3:7 anali kumuuzza Nikodemu kuti, “Uyenera kubadwa mwatsopano.” Ndiye Yohane akunena kuti munthu Wobadwa mwatsopano amapatsidwa chikhalidwe chatsopano ndipo moyo watsopano suchita ndipo sudzachitanso tchimo. Ichi, ndichifukwa chake mwana wolowerera sadakhazikike m’khola la nkumba popeza sanali nkumba, koma mwana wa atate, kotero kuti amalakalaka kukhala m’nyumba ya atate wake.

Kutsindika kuti ngati inu muli mwana wa Mulungu, mudzafuna kukhala m'nyumba ya Atate, kotero kuti simungakhazikike mutchimo.

Tsono mwina inu muli kakasi ndi mau akuti, “Yense Wobadwa kuchokera mwa Mulungu sachita tchimo...” Anthu ena amatanthauzira mau awa molakwika kwa wokhulupirirafe popeza lingaliro lake, silikunena za kuchita tchimo limodzi ayi, koma likunena zakuti wokhulupirira sakhazikika mutchimo. Mukumbukirani 1 Yohane 2:1, Mtumwi Yohane adanenetsa kuti, “Ndipo akachimwa wina, Nkhoswe tiri naye kwa Atate, ndiye Yesu Kristu wolungama.” Tchimo ndiko kutsutsana ndi chifuniro cha Mulungu ndiye Yohane akuti ife tiri ndi Nkhoswe kwa Atate, kotero kuti pamene inu mumvomereza machimo anu, Iye ndiye wokhulupirika ndi wolungama kuti atikhululukire machimo athu (Yoh.1:9). Apa Yohane amalankhula kwa akristu, kotero kuti amanena kuti akristu akhoza kuchimwa, koma pamene akunena kuti, aliyense amene ndiwobadwa mwa Mulungu sachimwa, akutanthauza kuti ngakhale mkristu achimwe, koma moyo wake watsopano sungalore kupitilira kukhala muuchimo ngakhale

zitabvuta motani. Ndikunena motsimikiza chomwechi, chifukwa ndimakhulupirira kuti moyo wanga mwa Yesu Kristu ndi wotetezedwa monga adanena Ambuye mwini pa Yohane 10:28, pamene adatsimikiza kuti, “Ndipo Ine, ndizipatsa moyo wosatha; ndipo sizidzaonongeka ku nthawi yonse, ndipo palibe munthu adzazikwatula m’dzanja langa.” Ili, ndilo ganizo lomwe Yohane akunena mundime ino kuti, “Yense Wobadwa kuchokera mwa Mulungu sachita tchimo, chifukwa mbeu yake ikhala mwa iye...”

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ilipano ndi yofunika kwambiri chifukwa tikanena za kubadwanso mwatsopano sitingonena kudza kutsogolo chabe kwa guwa, koma kutsimikiza mtima kuti ndinu Wobadwa mwa Mulungu. Ndiye ndikunenetsa kuti anthu onse, amene anabadwa mwa Mulungu ali wotetezedwa, komanso ndimakhulupirira kuti anthu onse amene amangonena kuti ndiwobadwa mwa Mulungu, koma pamene asanatsimikize mtima, iwowa moyo wawo ulipangozi. Kodi inu ndinu mwana weniweni wa Atate?

10. M'mene aoneka ana a Mulungu, ndi ana a mdierekezi: yense wosachita chilungamo siali wochokera mwa Mulungu; ndi iye wosakonda m'bale wake.

Pano tiyeni tiyambe ndi mau akuti ife, ana a Mulungu tiyenera kuyamba kuonetsa kuti ndife ana a Mulungu. Ndikunena mau amenewa chifukwa ana ambiri a Mulungu saoneka ngati ana a Mulungu. Iwowa amaoneka ngati kuti ndi ana a munthu wina, kapena ngati ana amasiye. M'dziko lapansi muli mabanja awiri ndipo anthu amene amaphunzitsa kuti Mulungu, ndiatate wa munthu wina aliyense, ndibodza losaneneka. Taonani Ambuye Yesu pa Yohane 8:44, adanena kwa akulu ansembe kuti, "Inu muli ochokera mwa atate wanu, mdierekezi ndipo zolakalaka zake za atate wanu, mufuna kuchita." Kutsimikiza kuti pali banja la Mulungu ndi banja la mdierekezi. Tamvani munthu wina adanena kuti ngati wokhulupirira angakwatire kapena kukwatiwa ndi wosakhulupirira ndiye kuti adzakhala pamkangano/pamabvuto ndi apongozi ake (mdierekezi).

Ndiye Yohane pano ationetsa zinthu ziwiri zomwe zingakuzindikiritsemi kuti ndinu mwana wa Mulungu. Tikunena

kuti Mulungu amadziwa mitima yathu ngati tikunena zoon kapena ndife wongodzitchula chabe kuti ndife ana ake. Koma taonani kuti anzathu sadziwa chimenechi, ndipo njira imodzi yomwe iwo angatidziwire ife, ndimoyo wa Mulungu womwe ungaonekere mwa ife. Sitikunena kuti moyo wa Mulungu ukhoza kuonetsedwa mwa mau anu chabe ayi, koma kudzera mwa momwe inu mukhalira m'dziko lino. Ndikunena kuti mkristu aliyense ali ndi makhalidwe ake akale mwa iye, kotero kuti ndikosatheka kuchotseratu makhalidwe amenewa panso pano. Koma chinthu chofunika kudziwa ndi chakuti makhalidwe athu atsopano ndiwo amene amapambana makhalidwe athu akale, kotero kuti zipatso za Mzimu monga chikondi, chimwemwe, mtendere, kupirira zimaonekera. Izi, zimaonekera pamene Mzimu wa Mulungu akhala ndi kugwira ntchito mwa inu, kuti inu mukhoza kubala chipatso chokoma.

Yohane akunenetsa kuti, “Yense wosachita chilungamo siali wochochera mwa Mulungu...” Nkhani ikuti kaya inu mudanena kuti ndinu mwana wa Mulungu, koma ngati simukhala m'moyo wa Mulungu, inu sindinu mwana wa Mulungu. Tikunena kuti inu

mukhoza kukhala achangu kapena wojjirika pachipembedzo, koma ngati mulibe chilungamo, sindinu mwana wa Mulungu.

Ndiye chizindikiro chachiwiri cha mwana wa Mulungu ndichakuti ngati inu muli mwana wa Mulungu, ndiye kuti mudzakonda m'bale wanu. Yohane akunena kuti inu muyenera kumakhudzidwa ndi kumathandiza munthu mnzanu makamaka m'bale wanu m'chikhulupiriro. Inu simuyenera kusunga mkwiyo pa m'bale wanu. Chikondi ichi, ndichomwe chimachokera mumtima kotero kuti chimachita ntchito. Koma tiyenera kutsegula maso athu chifukwa si onse amene ali abale ayi.

11. Pakuti uwu ndi Uthenga mudaumva kuyambira pachiyambi, kuti tikondane wina ndi mnzake.

Tsono Uthenga wachikondi udamveka kuchokera pachiyambi pamene Ambuye Yesu anakhala munthu pansi pano. Tere Yohane akungotsimikiza za chikondi chomwe Ambuye Yesu anaphunzitsa pa Yohane 13:35, pamene adati, "Mwa ichi, adzazindikira onse kuti muli akuphunzira anga, ngati muli nacho chikondano wina ndi mnzake." Kutsimikiza kuti chikondi ndicho chiyenera kukhala

chizindikiro cha anthu onse wotsatira Kristu. Chikondi chapa abale ndichimene chikusoweka pakati pathu lero lino.

12. Osati monga Kaini anali wochokera mwa woipayo, namupha m'bale wake. Ndipo anamupha Iye chifukwa ninji? Popeza ntchito zake zinali zoipa ndi za m'bale wake zolungama.

Pano mwina mwafunsa kale kuti, kodi bvuto la Kaini kuti aphe m'bale wake, linali chiyani? Yankho likuti Kaini anali ndi bvuto la kaduka kotero kuti ndilo linamfikitsa pakuti aphe m'bale wake Abele. Tsono nsanje ndi kaduka pakati pa akristu ndizinthu zina zomwe zikunyazitsa mpingo wa Kristu koposa zina zonse. Ndifuna muwerenge ndi anthu oimba angati, amene amachitira nsanje anzawo? Ndi atumiki angati a Mulungu amene amachitira nsanje atumiki anzawo? Tikunena kuti mijedu yochuluka mumpingo imachitika chifukwa cha kaduka. Nkhani ikuti Kaini anapha m'bale wake chifukwa chakuti Mulungu analandira nsembe ya m'bale wake nakana nsembe yake.

13. Musazizwe, abale, likadana nanu dziko lapansi.

Mtumwi Yohane pano, akunena kuti, wokhulupirira sayenera kuzizwa ndi kuona ngati kuti chinthu china chodabwitsa chachitika, pamene dziko silikuwalandira ayi. Popeza ndichinthu chomwe Ambuye Yesu adanena kale pa Yohane 15:18, pamene adati, “Ngati dziko lapansi lida inu, mudziwe kuti lidada Ine lisanayambe kuda inu.” Ndiye tikunenetsa kuti mwana wa Mulungu ayenera kudziwa kuti dziko lidzamuda ndithu. Tikunena kuti m’dziko lino muli m’chitidwe wonyazitsa mtanda wa Kristu, ndipo inu ndi ine, tiyenera kuonetsetsa kuti mtanda wa Kristu ukutetezedwa. Koma pamene titetezapo tiyenera kuonetsetsa kuti sitikuikapo mkwiyo wa umunthu wathu ayi. Kukanidwa kwa Kristu ndi kukanidwa kwathu kukhale kumodzi, osati inu mukhale ndi chifukwa chokhudza inu panokha ayi.

14. Ife tidziwa kuti tachokera kuturuka muimfa kulowa m’moyo, chifukwa tikondana ndi abale. Iye amene sakonda akhala muimfa.

Pano Mtumwi Yohane akunena kuti inu ngati wokhulupirira mukhoza kudziwa kuti ndinu mwana wa Mulungu. Koma ganizo lakuti inu simungathe kudziwa ndi cholakwa kwambiri, chifukwa

mau a Mulungu ndiwo amene akunena kuti inu ndi ine, tikhoza kudziwa ngati tiri ana a Mulungu kapena ayi. Ndiye funso likuti, kodi ife tikhoza kudziwa bwanji? Yankho likuti, inu mukhoza kukhala ndi chizindikiro chakuti ndinu mwana wa Mulungu pamene mulinacho chikondi chapa abale.

Wokondedwa anzanga apaulendo, Yohane akutsindika kuti iwo amene sakonda m’bale wake, ndiye akhala muimfa. Taonani awa, ndiwo anthu amene sakhudzidwa mkomwe ndi abale, koma inu ndi ine, tiyenera kukhala ndi mtima wokhudzidwa ndi abale. Tsono kuti inu mukhudzidwe ndi moyo wa abale anu, muyenera kukonda kuwerenga ndi kumva mau a Mulungu popeza ndiwo umboni wakuti inu munapulumsidwa. Kodi inu mulinawo umboni umenewu?

15. Yense wakudana ndi m’bale wake ali wakupha munthu; ndipo mudziwa kuti wakupha munthu ali yense alibe moyo wosatha wakukhala mwa iye.

Pano tikunenetsa kuti yense wakudana ndi m’bale wake ali wakupha munthu. Ambuye Yesu pa Mateyu 5:21-22, akuti, “Munamva kuti kunanenedwa kwa iwo kale, usaphe; koma Ine

ndinena kwa inu kuti yense wokwiyira m’bale wake wopanda chifukwa adzakhala wopalamula mlandu; ndipo amene adzanena ndi m’bale wake wopanda pake iwe, adzakhala wopalamula mlandu waukulu: koma amene adzati, chitsiru iwe: adzakhala wopalamula gahena wamoto.” Tsono mau awa ndi opweteka kwambiri kotero kuti ngati inu muli ndi mkwiyo mumtima mwanu pa m’bale wanu, zikutanthauza kuti inu ndinu wakupha munthu. Tamvetsani nkhani ikuti ngati inu muli ndi nkhwidzi ndi nsanje mumtima mwanu ndiye kuti muli ndi udani, ndipo udani ndiwo umene umafikitsa pakupha. Tsono mwa muyeso uwu, umene Mulungu anaika, zikutanthauza kuti alipo anthu akupha ambiri kunjira kwa ndende koposa omwe ali kale m’ndende.

Ndiye muverse 16, Mtumwi Yohane akunenetsa kuti Mulungu ndiye amene ali chitsanzo cha chikondi. Kunena kuti ife wokhulupirira, tiyenera kukondana monga momwe Mulungu amakondera ife tonse. Ndiye mwina mwafunsa kale kuti, kodi Mulungu amatikonda motani? Yankho likuti, inu ndi ine, tidziwa chikondi chake popeza adapereka moyo wake chifukwa cha ife.

Momwemonso inu ndi ine, tiyenera kupereka moyo wathu chifukwa cha abale.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyeni titsirize ndi mau akuti, pamene Yohane akunena kuti ife tiyenera kupereka chikondi chathu kwa abale monga momwe Iye anadzipereka kwa ife, akunena kuti inu ndi ine, tiyenera kufika pamlingo podzikhuthula pakutumikira Mulungu mwanjira yofalitsa Uthenga wake. Kodi inu mudafika pamlingo umenewu?

Lero tilekeza pano. Ndipo tinali kusanthula 1 Yohane 3:8-16, pamene timaona makhalidwe awiri a munthu wokhulupirira.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!